Muzipewa Kucheza Ndi Anthu a Makhalidwe Oipa

Malangizo: Chitani zotsatirazi muli pamalo opanda phokoso. Pamene mukuwerenga mavesiwo, yerekezerani kuti nkhaniyo ikuchitika inuyo muli pomwepo. Yesani kuona m'maganizo mwanu zimene zikuchitika. Mukhale ngati mukumva zimene anthuwo akulankhula. Yesani kumva mmene anthu a m'nkhaniyi akumvera mumtima mwawo.

Amene akutchulidwa kwambiri m'nkhaniyi: Dina, Sekemu, Yakobo, Simiyoni ndi Levi.

Chidule cha Nkhaniyi: Dina anagwiriridwa ndi Sekemu, azichimwene ake anakwiya kwambiri ndi zimenezi ndipo anakonza zokabwezera.

❶ ***ONANI NKHANIYI BWINOBWINO.—WERENGANI GENESIS 34:1-31.***

Kodi mukuganiza kuti Dina ankachita zotani ndi anzake a ku Kanani? _____

_____

_____

Polankhula ndi Dina, kodi mukuganiza kuti ndi nkhani zotani zomwe Sekemu "ankalankhula naye momunyengerera"? _____

_____

_____

Kodi mukuganiza kuti Yakobo ankamva bwanji pamene ankakalipira Simiyoni ndi Levi, zomwe zalembedwa m'vesi 30? _____

_____

_____

❷ ***FUFUZANI MOZAMA.***

Kodi mukuganiza kuti n'chifukwa chiyani Dina ankakonda kukacheza ndi ana akazi a Akanani? (Mwachitsanzo, kodi n'kutheka kuti anali ofanana pa zinthu ziti? Kodi ndi zinthu ziti zimene ankazipeza kwa anthu a ku Kanani zomwe mwina kwawo kunalibe?) _____

_____

_____

Kodi ndi makhalidwe ati a Sekemu amene Dina ayenera kuti ankakopeka nawo? (*Werenganinso vesi 3, 12, ndi* 19.) _____

_____

Kodi Baibulo limasonyeza bwanji kuti Dina sanachite kufuna kuti agone ndi Sekemu? (*Werenganinso vesi 2.*)

Kodi mukuganiza kuti Simiyoni ndi Levi anachita bwino kupha anthu a mumzinda umene Sekemu ankakhala, pobwezera zimene Sekemu anachita? N'chifukwa chiyani mwayankha choncho?

3 ***GWIRITSANI NTCHITO ZIMENE MWAPHUNZIRA. LEMBANI ZIMENE MWAPHUNZIRA ZOKHUDZA . . .***

Kufunika kosankha mwanzeru anthu ocheza nawo.

Kufunika kodziletsa kuti usabwezere ngakhale utakhala kuti wakwiya pa zifukwa zomveka.

MMENE MUNGAGWIRITSIRE NTCHITO MFUNDOZI.

Kodi mungadziteteze bwanji kuti anthu amene satsatira malamulo a Mulungu asakugwiririreni?

4 ***M'NKHANIYI, KODI NDI MFUNDO ITI IMENE YAKUKHUDZANI MTIMA KWAMBIRI, NDIPO N'CHIFUKWA CHIYANI?***



www.jw.org © 2011 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania